MACHITIDWE A ATUMWI

Mpingo M' Masiku Oyambirira

Malongosole dwe a Baibulo wogwiritsa ntchito panokha kapana pa gulu

Lolambedwa ndi

Fred Morris

Zatathanzidwa ndi Lapson Mbewi

MACHAPUTALA

1 Mpaka 12

Manna Publications

MANNA FOR ALL

KWA WOWERENGA

Ndemanga za Baibulozi zikunena chowonadi cha mawu a Mulungu. Mukhoza kugwiritsa ntchito mabukhuwa pophunzira Baibulo panokha kapena ndi anzanu pa gulu. Ngati mukuphunzira pa gulu ndi bwino aliyense wa pagulupo kukhala nalo bukhu lakelake ngati ndi kotheka.

WERENGANI' Pamene muwona chizindikiro ichi: Inuyo, kapena mtsogoleri wa gulu lanu werengani ndime ya Baibulo imene yasonyezedwa musanawerenge kuchokera mu bukhuli.

Pamene palembedwa : **'KAMBIRANANI'** pali mafunso amene mungathe kuthandizana pa gulu. Mafunsowo angathenso kuthandiza wowerenga kumvetsetsa bwino mavesi a Baibulo. Gwiritsani ntchito mafunsowo monga mayeso anu.

Cholinga cha ndemanga zimenezi ndi kuthandiza akhrisitu onse. Ophunzira Baibulo ndi Abusa adzawona kuti izi ndi zothandizanso kwambiri.

Ndemanga za Baibulozi zikupereka chowonadi cha Mulungu monga maziko a wokhulupirira onse. Atsogoleri a maphunzirowa apereke zitsanzo ndi umboni wochokera mu moyo wawo wa chi khri stu ndi zowoneka zina.

Illustrations copyright © Global Recordings Network. Used with permission.

Acts Part 1 Manna Bible teaching commentary © 2004, Fred Morris, Manna Publications (USA) Inc. All rights reserved

God has enabled us to print this title in the following countries:

Revised Worldwide English edition first published in the UK in 2004

Reprinted 2004 in Uganda (English). Reprinted 2005 in Uganda and Liberia (English)

Reprinted 2006 in Malawi (Chichewa) Myanmar, Sierra Leone & Nigeria (English), Sudan (Dinka)

Reprinted 2007 in Myanmar (English, Tiddim Chin and Khumi Chin); Ethiopia (Amharic); Malawi (Chichewa/Braille)

Reprinted 2008 in Ghana, Liberia and Zambia (English); Kosova (English/Albanian); Myanmar (Tiddim Chin)

Reprinted 2009 in Mozambique (Chichewa), D.R. Congo, Katanga (Kiluba, Kisongye and French); Nigeria (English); Togo (French); Pakistan (Saraiki)

Reprinted 2010 in Mozambique (Portuguese); Cambodia (Khmer); Cameroon (French and English); D.R. Congo, Katanga (Kiluba, Kisongye and French); Pakistan (Urdu), UK and Liberia (English) and in Mozambique (Portuguese)

Reprinted 2011 in India (Telugu, Tamil and English), Mozambique (Portuguese), Myanmar (Dai), Pakistan (Saraiki), Cameroon (English and French), Guatemala (Spanish)

Reprinted 2012 in Ethiopia (Oromo), D.R. Congo, Katanga (French and Kisongye), Burma (Falam Chin), Cameroon (French and English), India (Tamil)

Reprinted 2013 in D.R. Congo, Katanga (French), Cameroon (French)

Reprinted 2014 in D.R. Congo, Katanga (French)

Reprinted 2015 in Malawi (Chichewa Braille), D.R. Congo, Katanga (French), Cameroon (French), D.R. Congo, Kinshasa (French)

Reprinted 2016 in D.R. Congo, Katanga (French). 2018 in Cameroon (French), Malawi (Chichewa)

Reprinted 2019 in Malawi (Chichewa), Cameroon (French) and Cameroon for Eq. Guinea (Spanish)

Reprinted 2021 in Malawi (Chichewa, twice), D.R. Congo, Katanga (French, Kiluba plus Portuguese for Angola)

Reprinted 2022 & 2023 in Malawi (Chichewa)

Reprinted 2024: R.D. Congo, Katanga (French, Kiluba)

Reprinted 2025: Mozambique (Portuguese), Malawi (Chichewa)

MACHITIDWE A ATUMWI: Mpingo woyambirira
MAWU OTSOGOLERA

Bukhu la 'Machitidwe a Atumwi' linalembedwa ndi Luka. Luka anali kufuna kuti bwenzi lake Teofilo adziwe za Yesu. Nkhani imene adamuwuza ndi ya 'Uthenga Wabwino wa Luka,' bukhu lachitatu, mu gawo la Baibulo lochedwa Chipangano Chatsopano. Kenaka Dokotala Lukayu anamulemberanso Teofilo bukhu la Machitidwe a Atumwi.

Bukhu la Machitidwe a Atumwi likuyamba munyengo ya masiku angapo otsiriza a moyo wa Yesu pa dziko lino la pansi. Chiyambi cha Mpingo wa Yesu Khristu chinangotsatira nthawi imeneyi. Poyamba Luka akutiwuza m'mene Yesu ananyamukira kubwerera kumwamba kwa Atate Ake. Mukhoza kuwerenga za 'Kukwera ku Mwambaku' mu Marko 16:19; Luka 24:51; ngakhalenso mu Machitidwe a Atumwi 1: 9.

Luka anadziwa za zina zimene Yesu anachita powerenga ma uthenga a Mateyu ndi Marko. Iye anayankhulanso ndi anthu amene anakumana naye Yesu, kudzanso Akuphunzira ake a Yesu.

Chotero iye analemba bukhu la Machitidwe a Atumwi, nthano ya chiyambi cha mpingo wa Chikhirisitu. Luka anali wophunzira bwino. Analembanso mabukhu ena otchuka a Chihelene.

KODI LUKA ANALI NDANI?

Luka anali dokotala. Iye analinso mzake wa Paulo amene anayenda naye ma ulendo ake ena ofalitsa uthenga wa Yesu. Paulo anali kunena kuti Luka anali bwenzi lake la pamtima. 'Luka sing'anga wokondedwa' (Akolose 4 : 14). Paulo anali m'Yuda. Luka anali wa mtundu wa chi Helene (Greeks), motero iye sanali m'Yuda.

ZIMENE YESU ANANENA ASANAKWERE KUPITA KUMWAMBA

Yesu atawuka kuchokera kwa akufa, Akuphunzira ake khumi ndi m'modzi anabwerera ku Galileya. Yesu komanso mngelo uja anali atawawuza kuti iwo adzapite ku Galileya.

Ziphunzitso zotsirizira za Yesu zinali zotsatirazi:

1. Iye anawawuza kuti: 'Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi dziko lapansi' (Mateyu 28 :18).
2. Akuphunzira Ake apite ku dziko lonse lapansi ndi kutembenuzira anthu ambiri kwa Yesu. (Mateyu 28:19; Marko 16:15; Machitidwe 1:8).
3. Akuphunzira Ake awabatize okhulupirira m'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera (Mateyu 28; 19)
4. Akuphunzira Ake aphunzitse anthu zinthu zonse zimene Iye anawaphunzitsa (Mateyu 28:20)
5. Iye adzakhala ndi anthu Ake ku nthawi zonse (Mateyu 28:20).
6. Anthu amene akhulupirira mwa Yesu adzapulumutsidwa, koma iwo amene sakhulupirira mwa Iye adzalangidwa (Marko 16:16)
7. Iwo amene ali ndi chikhulupiriro nalalikira Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu adzawona zizindikiro ndi zozizwa kuchokera kwa Mulungu (Marko 16:17-18).

8. Zonse zonena za Iye mu zolembedwa zopatulika za Mose, Aneneri ndi Masalimo zidzakwanitsidwa (Luka 24:44).
9. Akuphunzira Ake adzawawuza anthu za Iye ndi kuwaphunzitsa za kutembenuka kusiya machimo awo kuti akhululukidwe (Luka 24:47).
10. Anthu amitundu yonse adzamva za dzina la Yesu (Luka 24:47).
11. Ntchitoyi, Akuphunzira Ake adzayiyambire ku Yerusalemu (Luka 24:47).
12. Akuphunzira Akewo adzadikire kufikira pamene Mulungu adzawatumizire mphamvu ya Mzimu Woyera kuchokera Kumwamba (Luka 24:49; Machitidwe 1:4)

Atanena zinthu zimenezi, Yesu anakwera kupita Kumwamba kukakhala ndi Atate Ake Mulungu. Uku kumatchulidwa 'Kukwera Kumwamba Kwa Yesu'. Kenaka Akuphunzirawo anabwerera ku Yesarulemu kukadikira Mzimu Woyera wa Mulungu kuti atsikire pa iwo.

Petro wophunzira wotsogolera potsatira Yesu, analemba mawu awa: "Yesu anafera machimo (anu). Anafa kukubwezeretsani inu kwa Mulungu. Thupi lake linaponyedwa ku imfa koma Mzimu Woyera anamubwezera Iye moyo. Yesu Khristu wakupulumutsani inu pokuwutsani kuchoka kwa akufa. Iye anapita Kumwamba ndipo ali kudzanja lamanja la Mulungu. Angelo, mphamvu ndi ulmuliro ziri mdzanja Lake' (1 Petro 3:18, 21,22).

Funsani Mulungu kuti akuthandizeni kumvetsetsa ndi kukhulupirira zinthu izi.

WERENGANI : MACHITIDWE 1:1–26

MPINGO, MZIMU WOYERA ASANAFIKE

Yesu atawuka kwa akufa, anakumana ndi Akuphunzira Ake nthawi khumi ndi ziwiri pa masiku makumi anayi (40) (Machitidwe 1:3). Iye anawaphunzitsa iwo zinthu zambiri za Ufumu wa Mulungu. Yesu asanakwere Kumwamba

anawalonjeza Akuphunzira Ake kuti adzawatumizira Mzimu Woyera kuti adzakhale nawo. "Sindikusiyani inu monga amasiye," Iye anatero. "Ndidzadza kwa inu' (Yohane 14:18).

Iye ananena nawonso kuti: 'Musachoke mu Yerusalemu, koma dikirani mphatso imene Atate Anga adakulonjezani inu. Mwandimva Ine ndikunena za Iye…mu masiku otsatirawa mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera' (Machitidwe 1:4, 5).

Yesu anawatuma Akuphunzira Ake kupita ku dziko lonse la pansi ndi kuphunzitsa zimene Iye anawaphunzitsa (Marko16:15). Iwo adzakhala Atumwi a Uthenga Wabwino ndipo adzapatsidwa mphamvu yakutha kukwaniritsa izi (1:8).

AKUPHUNZIRA KHUMI NDI M'MODZI ATCHEDWA APOSITOLI

Apositoliwa anasonkhana mu chipinda cha m'mwamba ku Yerusalemu, pamodzi ndi otsatira ena zana limodzi (100) ali kupemphera (1:12-150. Yesu anawawuza kuti adzatero (1:4). Anayenera kudikira ubatizo wa Mzimu Woyera (1:5). Adzadikire mu Yerusalemu kufikira mphamvu itadza pa iwo kuti adzawuze ena za Uthenga Wabwino wa Yesu (1:8).

Umboni wa kuwuka kwa Yesu Khristu

Atawuka kwa akufa, Yesu anawonekera kwa Akuphunzira Ake nthawi khumi ndi ziwiri :

1. Mariya akumana ndi Yesu (Marko 16:9; Yohane 20:14-17).
2. Mariya ndi Mariya mzake amuwona Yesu (Mateyu 28: 1,8–10).
3. Yesu alankhula ndi Petro (Luka 24:34).
4. Yesu pa njira ya ku Emau (Marko 16:12; Luka 24:13-32).
5. Yesu awonekera kwa Akuphunzira Ake amene anali kudikira muchipinda (Luka 24: 36-49).
6. Yesu awonekera makamaka kwa Tomasi (Yohane 20:26-29)
7. Yesu awonekera kwa Akuphunzira asanu ndi awiri pa nyanja ya Galileya (Yohane 21).
8. Yeasu aphunzitsa Akuphunzira asanu ndi m'modzi pa phiri (Mateyu 28:16)
9. Yesu akumana ndi Akuphunzira pa chakudya (Machitidwe 1:4).
10. Yesu awonekera kwa Akuphunzira mazana asanu (1Akorinto 15:6).
11. Yesu awonekera kwa Yakobo ndi m'bale wake (1Akorinto 15:7).
12. Yesu awonekera kwa nthawi yotsiriza

Yesu atatengedwa kupita Kumwamba (1:9) Angelo awiri anawuza omutsatira za Yesu motere: 'Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kuchokera kwa inu, adzadza momwemo konga munamuwona ali nkupita Kumwamba' (1:11). Ichi ndi chifukwa chake Akhristu amakhulupirira kuti Yesu adzabweranso tsiku lina.

Kwa masiku angapo otsatira a Yesu anakhala m'nyumba ali kupemphera ndi kukambirana podikira kubwera kwa Mzimu Woyera. Iwo anadzikonzetsera ndi kuyembekezera. Anasankhanso wina wolowa m'malo mwa Yudasi kuti akawathandize 'kulalikira za kuwukanso kwa Yesu' (1:22). Mphamvu ya Mzimu inali isanadze kwa iwo. Komabe iwo anayanjana mu chikondi ndi cholinga chimodzi. Abale a Yesu anali pakati pawo (1:14)

MULUNGU ASANATUMIZE MZIMU WOYERA

Machitidwe 1:12-26 amatiwuza kuti Akuphunzira a Yesu anakumana Mzimu Woyera **asanatumizidwe** kwa iwo.

- Okhulupirirawo, amuna ndi akazi anali kukumana kawirikawiri (1:14).
- Anali kukumana mwa umodzi ndi kupemphera (1:14, 24).
- Petro anali mtsogoleri wawo (1:15). Onaninso Mateyu 16:17-19.
- Anali kumvera mawu a muzolembedwa zopatulika (1:20).
- Anachita masankho kusankha wolowa m'malo mwa Yudasi (1:21-26)
- Anapemphera kwa Mulungu kuti awathandize kusankha (1:24).

Nthawi ya misonkhano imeneyi n'kuti mphamvu ya Mzimu Woyera isanadze.

MAFUNSO : Kodi Mzimu Woyera akugwira ntchito mu misonkhano ya tchalitchi chanu? Kodi inu mukuyesayesa kuchita bwino panokha popanda mphamvu ya Mulungu kukutsogolerani? Kodi muyenera inu kupempha Mulungu kuti akutsogolereni mwa Mzimu Woyera? Kodi mumakhulupirira kuti Mzimu wa Mulungu amagwira ntchito pamene anthu asonkhanba ndi kupemphera?

KAMBIRANANI :

1. Kodi ndi anthu angati amene anamuwona Yesu atawuka kwa akufa (1 Akorinto 15: 5-7)?
2. Yesu anaphunzitsa zokhudza chiyani asanakwere kupita Kumwamba (1:3)? Chifukwa chiyani?
3. Kodi Yesu anawalamula Akuphunzira Ake kuchita chiyani (Machitidwe1:4)?
4. Angelo ananena chiyani kwa Akuphunzira (1:11)? Izi zikutanthawuza chiyani?
5. Ndi gulu liti la anthu linali kukumana mu Yerusalemu ndi kupemphera (1:12-15)?
6. Ndi chifukwa chiyani kuli kofunika kuti okhulupirira adzigwirizana (1:14)? Chimachitika ndi chiyani ngati okhulupirira akumana pamodzi ndi kupemphera?

WERENGANI: MACHITDWE 2:1-13

YESU ATUMIZA MZIMU WOYERA

Patatha masiku khumi Yesu atakwera Kumwamba, okhulupirira zana limodzi ndi mphambu makumi awiri (120), anali kudikira ndi kupemphera m'mamawa. Zodabwitsa zinaoneka. Iwo anamva phokoso lalikulu nawona malilime ogawanikana owoneka ngati moto. Ndipo motowo unatera pa aliyense wa iwo amuna ndi akazi, payekhapayekha. Izi zitachitika aliyense wa iwo anagwidwa ndi Mzimu Woyera nayamba kuyankhula mu zinenero zosiyanasiyana popanda kuziphunzira (2:4). Kunali chimwemwe ndi kuzizwa kwakukulu.

Iyi inali nthawi ya Phwando la Pentekosite pamene Ayuda anali kusonkhana pamodzi kudzathokoza Mulungu chifukwa cha zokolola zawo. Ayuda ambiri anali kufika ku Yerusalemu kuchokera ku mayiko ena (Machitidwe 2:9-11) kudzapembedza Mulungu. Choncho mu Yerusalemu munadzaza zikwizikwi za anthu.

Anthu amenewa adawamva otsatira a Yesuwa akulemekeza Mulungu mu zinenero zosiyanasiyana. Aliyense anali kumva za 'zozizwa za Mulungu' mu chinenero chawo (2:8-11). Iwo anadabwa kwambiri (2:12). Mzimu Woyera anapatsa Akuphunziwa mphamvu yoyankhula mopanda mantha. Akuphunzira anakumbukira zimene Yesu adawawuza kuti: 'Inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera asanapite masiku ambiri' (1:5). Tsopano zinali kuchitika.



KAMBIRANANI:

1. Kodi Mzimu Woyera ndi ndani? (Yohane 14:16-17)
2. Ndi chifukwa chiyani Yesu anatumiza Mzimu Woyera wa Mulungu? (Luka 12:11-12; Machitidwe1:8; 1 Yohane 2:20)
3. Kodi Mzimu Woyera adafikira wokhulupirira aliyense (2:3, 4)?
4. Kodi Mzimu Woyera adawasintha motani okhulupirira a Yesu aja (2:3-4)?
5. Nanga khamu losonkhana lija Mzimu Woyera adalikhudza bwanji (2:6-7; 11-13)
6. Nanga inuyo, Mzimu Woyera amakukhudzani motani m'moyo wanu?

WERENGANI: MACHITIDWE 2:14–47

PETRO AYANKHULA KWA ANTHU

Petro anayima nayankhula ndi khamu lidasonkhanalo. Mzimu Woyera adamupatsa iye mphamvu yakutha kutero. Anthu amenewa anali kudziwa zolembedwa zopatulika za mu Chipangano Chakale choncho Petro anagwiritsa ntchito uthenga wa mneneri Yoweli (2:16; Yoweli 2: 28 –32).



Iye anawawuza anthuwo kuti Mulungu, anakwaniritsa lonjezo lake limene adalipanga kudzera mwa mneneri Yoweli. 'Mulungu watumiza Mzimu Wake.'

Petro anayankhula motere:

- Yesu anali munthu amene Mulungu anakondwera naye (2:22)
- Inali nzeru ya Mulungu kuti Yesu adzafe (2:23)
- Timawuzidwa zimenezi mu zolembedwa zopatulika (2:25)
- Mulungu anamudzutsa Yesu kwa akufa (2:32)
- Yesu tsopano ali ndi Mulungu Atate (2:33)
- Ndi Iyeyo Yesu amene watumiza Mzimu Woyera (2:33)

MZIMU WOYERA NDI M'MODZI WA ATATU MU 'UTATU WA MULUNGU'



Baibulo siligwiritsa ntchito liwu lakuti 'Utatu' koma limatiwuza za atatu amene apanga Mulungu m'modzi. (Onani Mateyu 3:16-17; 4:1; 28:19; Machitidwe 2:38-39; Agalatiya 4:6; Aefeso 1:3, 13; 2 Akorinto 13:14; Chivumbulutso 4:1-3; 5:6-10).

Ambiri satha kumvetsa chiringanizo ndi ganizo lakuya la 'Atatu mwa Mulungu m'modzi.' Pempherani kuti mulandire chidziwitso chakutha kumvetsetsa chiphunzitso cha 'Utatu wa Mulungu' kuti muthenso kuthandiza ena kumvetsa.

Akhiristu oyambirira mu zaka chikwi ndi mazana asanu ndi anayi (1900) zapitazo anali kugwiritsa ntchito chizindikiro chokhala ndi magawo atatu olukana pofuna kumvetsetsa za 'Utatu wa Mulungu.' Ichi chinali kutchedwa 'Celtic Rope or Knot' (Chingwe Chomangana' mwachidule) Zigawo zonse zitatu za chingwechi ndi zolumikizana kupanga chinthu chimodzi, monganso momwe Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera ali amodzi.

Mzimu Woyera anali ndi Mulungu Atate pa chiyambi cha dziko (Genesis 1:2). Yesu analinso ndi Mulungu Atate pa chiyambi cha dziko (Yohane 1:3; 1 Akorinto 8:6; Ahebri 8:12).

Mzimu Woyera wa Mulungu anatumizidwa ndi Yesu kukathandiza otsatira Ake kukhala moyo wangwiro (Luka 24:49; Yohane 14:16–17; Machitidwe 1:4–5; Aroma 8: 9). Mulungu anapereka lonjezo limeneri mu zolembedwa zopatulika zaka mazana asanu ndi limodzi (600) zinthuzi zisanachitike (Ezekieli 36:27; 39:29). Yohane Mbatizi anadzatsimikizanso kuti izi zidzachitika (Mateyu 3:11).

Mulungu analonjeza kuti adzapereka Mzimu Wake kwa okhulupirira amene amufunsa kutero (Luka 11:13; Machitidwe 2:38). Mzimu Woyera akugwira ntchito nthawi zonse. Mzimu Woyera akuthandiza anthu kuzindikira machimo awo. Iye amalozera anthu kwa Yesu kuti akathandizidwe ndi kukhululukidwa.

Mphamvu ya Mzimu Woyera imapereka zizindikiro ndi zozizwa (Machitidwe 2:2–4; 4:31; 8:6–8).

Kenaka Petro anawawuzanso kuti: 'Yesu yemweyu amene inu mudamupachika, Mulungu adamuyesa Ambuye ndi Khristu (2:36). Petro anawawuza iwo kuti Yesu ndiye Khristu, Mesiya Wolonjezedwa, amene anabwera kudzapulumutsa dziko lapansi ku machimo. Iwo anali kuganiza kuti anathana naye Yesu pomukhomera pa mtanda, koma sizinali choncho ayi.'

Ambiri akhamulo atamva anachita manyazi (2:37). Iwo anafuna kudziwa kuti angachite chiyani kuti apulumutsidwe kuchoka ku njira zawo zochimwa.

UTHENGA WACHIPULUMUTSO: WOMASULA KU UCHIMO

Anthu ambiri anakhulupirira zimene Petro ananena. Iwo anakhulupirira kuti Yesu anafa chifukwa cha machimo awo. Iwo anakhulupirira kuti iyi inali nzeru ya Mulungu. Anakhulupiriranso kuti Yesu anali Khristu, Mesiya wochokera kwa Mulungu (2:36)

Petro anawawuza anthuwo chimene anayenera kuchita kuti apulumutsidwe ku machimo awo. (2:38). 'Lapani, batizidwani, yense wa inu mdzina la Yesu…kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu. Inunso mudzalandira Mzimu Woyera.'

Petro ananenso kuti, 'Lomjezo iri liri kwa anthu onse akutali, onse amene Ambuye Mulungu wathu adzayitana' (2:39) Chipulumutso sikuti ndi cha ayuda okha ndi mabanja awo ayi, koma ndi cha anthu onse kwina kuli konse kume Mzimu wa Mulungu akuwayitana. Anthu oposa zikwi zitatu anapulumutsidwa tsiku limeneri (2:41). Izi zinachitika Mulungu atatsika mwa mphamvu ndi moto (2:2-3). Mzimu wa Mulungu adaperekedwa kwa amuna ndi akazi amene adakhulupirira mwa Yesu.

KAMBIRANANI:

1. Kodi anthu adamva bwanji ndipo adanena chiyani (2:37)?
2. Ndi chifukwa chiyani anthuwa adamva m'mene anali kumveramu (Yohane 16:8)?
3. Nanga Petro ananena kuti anthuwa ayenera kuchita zinthu ziwiri zotani (2:38)?
4. Kodi Petro anawawuza anthuwo kuti Mulungu adzawachitira zinthu ziwiri zotani (2:38)?
5. Kodi mphatso ya chipulumutso ya Mulungu ndi ya anthu otani (Machitidwe 2:39)?

M'MENE UNALIRI MPINGO

MZIMU WOYERA ATABWERA

Pa Machitidwe 2:42 –47 timawerengapo zakuti omutsatira Yesu atsopano amakumana pamodzi atapatsidwa Mzimu Woyera ndi Yesu:

- Okhulupirirawa anali kukumana tsiku liri lonse mu Kachisi wa ku Yerusalemu (2:46).
- Iwo anali kupemphera pamodzi (2:42).
- Iwo anali kusonkhana pamodzi mwa ubale ndi okhulupirira ena (2:42; 44).
- Atumwi amene anali kuwatsogolera analinso kuwasamalira (2:42–43).
- Okhulupiriwa anali kumvetsera ndi kuphunzira zimene atsogoleri awo anali kuwaphunzitsa (2:42)
- Iwowa anali kugawana zimene anali nazo wina ndi mzake ngakalenso kugulitsa katundu wawo wina kuti athangatire okhulupirira anzawo (2:44–45).

- Iwo anali kunyema mkate pamodzi mu nyumba za wokhulupirira anzawo- pokumbukira imfa ya Ambuye Yesu Khristu monga Iye adawaphunzitsira pa Mgonero Wake wotsiriza (2:42, 46; Luka 22:19).
- Iwo anadziwa kuti Mulungu anali pafupi nawo (2:43).
- Atumwi anachitazozwizwa zambiri mu dzina la Yesu (2:43).
- Iwo anali kukumananso mu m'malo osonkhaniranapo anthu ngakhalenso mu nyumba zawo (2:46).
- Iwowatu anali wokonda ndi wodzichepetsa, (2:46) okondana wina ndi mzake komanso okonda Mulungu.
- Iwo anali kulemekeza Mulungu (2:47).
- Tsiku lina liri lonse anthu ambiri anali kukhulupirira ndi kulandira Yesu (2:47).

UBATIZO

Yesu anawuza otsatira Ake kuti pali mitundu iwiri ya ubatizo. 'Yohane anabatiza ndi madzi. Koma . . . inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera' (Marko 1:8; Machitidwe 1:5). Petro analiwuza khamu lija zimenezi pa Machitidwe 2:38.

UBATIZO WA MADZI: Chipangano Chatsopano chikunena za ubatizo pamene Yohane M'batizi adadza kudzakonza njira ya Yesu (Marko 1:4). Iye anawawuza anthu kuti:

'Tembenukani ndi kusiya machimo anu, ndipo batizidwani kuti mukhululukidwe ndi Mulungu.' Yesu anawawuza otsatira Ake kuti adziwabatiza iwo amene akhulupirira mu madzi, m'dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera (Mateyu 28:29). Akuphunzirawo adachita zimene Yesu anawawuza (Machitidwe 2:41). Kumizidwa m'madzi kumapereka chithunzithunzi chakuti tasiya machimo athu ndipo takhululukidwa. Choncho 'timafa' ku uchimo ndipo 'timakwiriridwa.' Komano kupyolera mu mphamvu ya kuwuka kwa Khristu 'timawukitsidwa' kulowa m'moyo watsopano.

KUBATIZIDWA NDI MZIMU: Izi zinachitika kwa nthawi yoyamba pa Machitidwe 2:2-3, pa Phwando la Pentekosite. Mzimu Woyera adatsika- monga malirime a moto- pa okhulupirira pamene anali kupemphera. Zitatha izi Petro anawuza okhulupirira ongotembenuka kumenewo kuti nawonso akhoza kulandira mphatso ya Mzimu Woyera (8:15–17).

Pa tsiku limene Mzimu Woyera anatsikali, Atumwiwa adabatiza onse otembenuka mu madzi (2:41); ndipo awa anali anthu pafupifupi zikwi zitatu. Okhulupirira aliyense anabatizidwa mwa madzi ndiponso mwa Mzimu.

KAMBIRANANI:

1. Kodi kubwera kwa Mzimu Woyera, kudawasintha bwanji anthu amenewa? (Fananitsani kapena kusiyanitsa Machitidwe chaputala 1 ndi 2).
2. Tingathe bwanji kukhala ndi misonkhano ya tchalitchi monga anali kukhala nayo anzathuwa pa Machitidwe 2:42–47?
3. Kodi otembenuka atsopanowa anali kukhala moyo wotani (2:42–47)?
4. Kodi chinawawonekera ndi chiyani okhulupirira atsopanowa (2:43,47)?
5. Konga anthu amene sali Akhristu amatha kumuwona Mzimu Woyera akugwira ntchito m'moyo wanu ndi mu tchalitchi chanu?

WERENGANI: MACHITIDWE 3:1–26

PETRO NDI YOHANE MU KACHISI

Anthu amene adakhulupirira mwa Yesu Khristu wa analibe nyumba ya tchalitchi, choncho anali kukumana mu nyumba zawo kapenanso ku kachisi kuti apembedze Mulungu. (2:46).

Tsiku lina Petro ndi Yohane anapita ku Kachisi. Mwamuna wina wolumala anakhala pa chipata cholowera mu Kachisi kuti apemphe ndalama. Popeza anali wolumala, sanali kuloledwa kulowa mu Kachisi. Iye anatansa dzanja lake kwa Petro mopempha. Petro anamuwuza iye kuti 'Siliva ndi golide ine ndiribe, koma ndikupatsa chimene ine ndiri nacho.' Ndipo kenaka anati: 'M'dzina la Yesu Khristu, nyamuka nuyende!' (3:6).

Petro anatansa mkono wake namuthandiza kunyamuka. Nthawi yomweyo wolumalayo anachira. Iye anayimirira nawatsatira Petro ndi Yohane mu Kachisi. Iye anali kuyenda ndi kudumphadumpha ndi kulemekeza Mulungu! Anali atachira! Tsopano anali okhoza kulowa mu Kachisi ndi kuleka kupemphetsa! Anthu ambiri anathamanga kudzamuwona ndipo anamumva akunena zimene zinamuchitikira. Anali wozizwa kwambiri kuwona kurti anali kuyenda bwino lomwe!

'Amuna inu a mu Israeli muzizwa naye bwanji ameneyo?' Petro anawafunsa. 'Munthu ameneyu wachiritsidwa mwa chikhulupiriro pa dzina la Yesu' (3:16). Petro anawakumbutsa anthuwo kuti iwo adamupachika Yesu. 'Inu mudamupereka Yesu kuti akaphedwe…Inu munamunenera Iye zonama…Inu mudapempha kuti wambanda amasulidwe m'malo mwake… Inu mudapha Iye wakutha kupereka moyo. Koma Mulungu adamuwukitsa Iye kwa akufa' (3:13-15). Ndipotu chinali chikhulipiriro mwa Yesu chimene chidachiritsa munthu uyu' (3:16). Yesu ali ndi mphamvu yakhoza kuchita zimenezi chifukwa Iye ndi Mwana wa Mulungu.

Petro adawanenanso zolembedwa mu zolembedwa zopatulika. Aneneri onse adanenera za m'mene Khristu (Mesiya) ati adzanzunzidwire ndi kufa (3:18,24). Mu Malamulo opatsidwa kwa Mose, mudalembedwa kuti ochimwa onse ayenera kufa, 'Pakuti mphotho ya uchimo ndi imfa. . .' (Aroma 6:23). Koma Yesu anadza ndi kufa m'malo mwathu. Iye adatilonjeza moyo osati imfa! Yesu Khristu akadatha kupulumutsa anthu ku machimo awo powafera m'malo mwawo.

YESU ADAFA KUPULUMUTSA DZIKO LA PANSI

Petro adagwiritsa ntchito kuchiritsidwa kwa munthu wolumalayu, ndi kuwawuza anthu Uthenga Wabwino waYesu. Tembenukani ndi kusiya machimo anu ndipo mubwerere kwa Mulungu, pamenepo machimo anu adzafafanizidwa. (3:19). Mulungu adamukweza Yesu… kuti akudalitseni pokubwezani aliyense wa inu kuchoka ku njira zanu zoyipa' (3:26). Pafupifupi zaka zikwi ziwiri (2000) zapitazo, izi zisanachitike, Mulungu adapanga lonjezano ndi Abraham lakuti: 'ndidzakusandutsa iwe kukhala mtundu wawukulu [Israeli]…ndipo anthu onse a padziko adzadalitsidwa mwa iwe' (Genesis12:2-3). Tsopano Petro anazindikira kuti lonjezanoli linali kukwaniritsidwa. Anthu ochokera ku mayiko onse a pa dziko anali atasonkhana mu Yerusalemu kudzapembedza Mulungu (Onani mapu pa tsamba 13). Iwo anamva za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Anthu wochokera kumbali zosiyanasiyana anapulumutsidwa ndi kudalitsidwa. Izi zinali kuchitika tsiku ndi tsiku kuchokera pa tsiku loyamba la Penetekoste. Mphamvu ya Mulungu yopulumutsa imatha kuchita zotere. Mphamvu imeneyi timayitchula kuti 'Mphamvu ya Pentekoste' chifukwa mphamvu ya Mzimu Woyera inatsika pa tsiku la Pentekoste. Ife tikalalikira za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, mphamvu ya mawu a Mulungu idzasintha miyoyo ya anthu. Mulungu ndi wachifundo. Iye amakhululukira machismo a wanthu mwa nsembe yoperekedwa ndi Yesu Khristu.

Uthengawu ukutikhudzanso ife amene. Yesu adafa kupulumutsa ife. Ifenso titha kuwawuza ena za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu ndi kuchitira umboni mphamvu ya Mulungu ikusintha miyoyo. Ifenso tikhoza kukhala mboni za Yesu kuli konse kumene ife tikukhala ku 'malekezero onse a dziko.'(1:8)

WERENGANI: MACHITIDWE 4:1–37

ATSOGOLERI A CHIPEMBEDZO AFUNA KULEPHERETSA UTHENGA WABWINO

Petro ndi Yohane adaphunzitsa anthu mu Kachisi. Iwowa anali kuwawuza kuti Yesu adawuka kuchokera kwa akufa. Izi zinakwiyitsa atsogoleri a Chiyuda, makamaka Asaduki amene sanali kukhulupirira za mdzukiro. Asadukuiwa adadza ndi asilikari a Mkachisi nagwira Petro ndi Yohane.

Iwo adawayika Atumwiwa mu nyumba ya ndende. Pa nthawi imeneyi panali amuna oposa zikwi zisanu amene anakhulupirira (4:4) ndinso azimayi miyandamiyanda. Zonsezi zinachitika chifukwa cha kuchiritsidwa kwa munthu m'modzi. Umboni wa munthu m'modzi ameneyu unathandizira Petro ndi Yohane kulalikira Uthenga Wabwino zimene zinachititsanso kuti anthu ambiri akhulupirire mwa Yesu Khristu.

Tsiku lotsatira Petro ndi Yohane anawatengera ku bwalo la milandu. Anawafunsa iwowa mafunso awiri ofunika pa nkhani ya kuchiritsidwa kwa munthu wolumala uja kuti: 'Kodi mwachita ichi ndi mphamvu yanji?' Funso lina linali lakuti:'Mu dzina lanji mwachita ichi?' (4:7).

Mafunso amenewa adamuthandiza Petro kuwawuza iwo za Yesu. Iye adayankha molimba mtima kuti: 'Mulungu adamuwukitsa Yesu kwa akufa ndipo kudzera mdzina la Yesu munthu uyu wachiritsidwa' (4:10).

Petro ndipo adapereke uthenga womwe uja anawulalikira poyambawu molimba mtima chifukwa mphamvu ya Mzimu Woyera inali ndi iye (4:8). Iye anati:

- Yesu adafa chifukwa cha machimo a wanthu (4:10).
- Yesu adawuka kwa akufa (4:10).
- Zolembedwa zopatulika zinaneneratu kuti izi zidzachitika (4: 11).

Mulungu adamukhazikitsa Yesu kukhala Mutu kapena 'mwala wa pa ngodya' mu mpingo Wake (Masalimo 118: 22, 23). Ndipo Mulungu adamuyitana Petro kuti amange Mpingo Wake (Mateyu 16:18) Atsogoleri achipembedzowa anayenera kugwira ntchito ndi Petro kumphunzitsa anthu kuti Yesu ndi Mfumu. Koma iwo adakana kukhulupirira Mesiya wawo ndipo adamupha. Nawa tsopano ali kukana zimene Petro anali kuwawuza.

Petro adachenjeza bwalo la mirandulo kuti 'Palibe chipulumutso mwa wina ali yense pakuti palibe dzina lina …..limene tiyenera kupulumutsidwa nalo' (4:12).

Asaduki adafunsana kuti: 'Ndi chiyani chikupangitsa anthu wambawa kulimba mtima chotere? Chozizwachi chinatheka bwanji? Kodi anthu amenewa titani nawo? (4:16). Kenaka adawawuza Petro ndi Yohane kuti: 'Musayankhulenso za dzina limeneri' (4:18). Koma Petro ndi Yohane anati iwo apitirrabe kuyankhula za dzina limeneri (4:20).

KAMBIRANANI :

1. Kodi Petro ndi Yohane adagwidwa chifukwa chiyani (4:2)?
2. Kodi Asaduki adawalamula iwo kuti asachite chiyani (4:18)?
3. Ndi mphamvu yanji imene inali kugwira ntchito yochiritsa ndi kulalikira (3:6, 16, 26; 4:2, 4)?
4. Kodi Petro ndi Yohane adamvera Mulungu kapena Asaduki (4:19)?
5. Ndi chifukwa chiyani bwalo la mirandu linayesa kuletsa kuphunzitsa za Yesu?

MPINGO NDI PEMPHERO PA NTCHITO

Zitatha izi, Petro ndi Yohane anabwerera nakalumikizana ndi okhulupirira ena. Kumeneko anapemphera ndi kulemekeza Mulungu pamodzi. Mu mapmphero awo anatchula za 'Wodzozedwayo' amene ali Khristu; Mesiya wotumizidwa ndi Mulungu. Zaka mazana ambiri izi zisanachitike, Mfumu Davide analemba za kubwera kwa Yesu. Iye anati mafumu a dziko lapansi andi olamulira amitundu adzakwiya chifukwa cha Yesu (4:25–26; Masalimo 2: 1-2).

Mulungu amadziwa zimene ziti zidzachitike. Iye adamuvumbulutsira Mfumu Davide kuti alembe zimenezi. Ife sitiyenera kuwopa ayi. Mulungu amadziwa zonse!

Pamene Petro ndi Yohane anali pa mavuto, mpingo udapemphera. Kodi iwo adakhumudwa? Kapena anali ndi nkhawa? Ayi!

- Iwo adalemekeza Mulungu mu mapemphero awo (4:24)
- Iwo anali kuwerenga zolembedwa zopatulika (4:25–26).
- Iwo anali kukumbukira m'mene Yesu adanzunzidwira ndi kulangidwa (4:27).
- Iwo anali kukhulupirira kuti Mulungu anali ndi Chikonzero Chake (4:28).
- Iwo anali kumupempha Mulungu kuti awapatse kulimba mtima (4:29).
- Iwo adapempha zozizwa zambiri mu dzina la Yesu (4:30).

Pa nthawi yonseyi, Akhristuwa anali kukumana mu nyumba zawo. Iwo anali kusamalirana ndi kuthandizana wina ndi mzake. Komanso anali kugawana zimene anali nazo ndi kuchita zonse mogwirizana. Mzimu Woyera anayamba kuwapatsa ntchito mu miyoyo yawo (4:32). Ena anali kugulitsa minda yawo (malo awo) ndi kubweretsa ndalamaza kwa Atumiki a Mulungu (Apositoli) 94:36 –37). Anali kuchita izi kuti athe kuthandiza ena mwa okhulupirira amene anali osawuka (4:35). 'Kwa ulere mwalandira, kwa ulere patsani' anatero Yesu (Mateyu 10:8).

KAMBIRANANI :

1. Kodi chinali kuwalimbikitsa okhulupirira kuti apemphere kwa Mulungu chinali chiyani (4:23–24)?
2. Anali kuwerenga chiyani pamodzi, mokweza (4:25–28)?
3. Ndi chifukwa chiyani atumikiwa adamupempha Mulungu kuti awapatse kulimba mtima (4:29)?
4. Kodi kunali kofunikira bwanji kutchula dzina la Yesu (4:30)?
5. Nanga chinali kuchitika ndi chiyani iwo akapemphera (4:31)?
6. Tafotokozani mu mawu anu za moyo wa Akhristu woyambawa (4:32–37).

WERENGANI: MACHITIDWE 5:1– 42

MULUNGU ALANGA UCHIMO

Mulungu amakondaanthu ochimwa koma adana nalo tchimo lathu. Ichi ndicho chifukwa chimene anatumizira Yesu kudzafera anthu ochimwa. Mulungu amafuna ife tidzikhala moyo womusangalatsa iye.

Hananiya ndi mkazi wake Safira anagulitsa mbali ina ya munda wawo. Iwo anakapereka ndalama zina kwa Petro koma anamunamiza. Ichi chinali 'chinyengo' ndipo iri ndi tchimo. Iwo adamuwuza Petro kuti ndalamazo zinali zonse zomwe analandira pa malonda amunda wawo. Petro sananene kuti kusunga mbali ina ya ndalamazo linali tchimo koma kunena bodzako ndiro linali tchimo. Anali ndi ufulu kuchita china chiri chonse chimene akanafuna ndi ndalama zawo, koma sanayenera kunama ayi. (5:4)

'Satana anadzaza mtima wako… sunanamize anthu koma wanyenga Mzimu Woyera (5:3). Petro atanena mawuwa Hananiya anagwa pansi nafa. Patangopita ma ola atatu mkazi wake anatulukirananenanso bodza lomwe lija. Petro anati: 'Munapangana pamodzi bwanji bwanji kuyesa Mzimu Wa Ambuye?' Nayenso anagwa anagwa pansi nafa. Anthu ena onse anachita mantha nawopa kunena bodza (5:11).

Tsiku ndi tsiku anthu ambiri anali kutembenuka ndi kukhulupirira mwa Ambuye Yesu. Okhulupirirawa anali kusonkhana pamodzi pa bwalo losonkhanirapo cha kum'mawa kwa Kachisi wa ku Yerusalemu (5:12). Anthu anali kuchokera mtalimtali kudzamva uthenga ndi kudzawona zodabwitsa zochitika mu dzina la Yesu. Izi zinakwiyitsa akuluakulu a Chiyuda ndi Asaduki ena amene anayamba kuchita nsanje, nawaponya Atumwi mu ndende (5:18).

MULUNGU ATUMIZA M'NGELO WAKE

Mkati mwa usiku Mulungu anatumiza mngelo amene anatsekula makomo a ndende nawatulutsa (5: 19)

Mngeloyo anawawuza kuti: 'Pitani ndipo imirirani mu Kachisi nimulankhule kwa anthu onse mawu a Moyo umene.' Iwo anamvera napitanso ku Kachisi kukaphunzitsa anthu (5:21). Uthenga Wabwino wa Yesu umapereka moyo watsopano kwa ife tonse – tinachimwa- tonse ndife wochimwa (Yohane 17:3; Aroma 3:23).

Pamene anthu amva uthenga wa Mulungu,ndipo chikhulupiriro chimakula mumitima mwawo, amawulula mphulupulu zawo ndi kubwereranso kwa Mulungu. Iwo amakhulupirira Uthenga Wabwino ndipo Mulungu amawakhululukira iwo mwa chisomo ndi chifundo (Aroma 10:10; Aefeso 2:8 -9). Awa ndi 'Obadwanso mwatsopano'. Amakhala tsono 'Cholengedwa chatsopano' mwa Yesu (2 Akorinto 5:17). Munthu wokonzedwanso! Ife timakhululukidwa chifukwa cha nsembe ya Yesu. Iye adafa m'malo mwathu.

M'mawa wotsatirawo atsogoleri a Chiyuda anasonkhana pamodzi ku bwalo. Iwo anatumiza nthumwi kuti zikatenge a mndendewo koma nthumwizo zinabwerera ndi kuwawuza kuti: 'Tinapeza makomo a ndende ali

SATANA AMAYESAYESA KUTINYENGA IFE

Hananiya ndi Safira mkazi wake, ananama pamaso pa Mulungu ndi pamaso pa anthu Ake poyesa kunyenga Atumwi (5:1, 28). Mchitidwe umenewu udalangidwa kotheratu popeza chinyengo, mabodza ndi dyera si khalidwe la umulungu. Makhalidwewa amalepheretsa Mzimu Woyera kugwira ntchito Yake, choncho madalitso sabwera kuchokera kwa Mulungu. Kunama kuli ngati kuwabera anthu ndipo timachitcha 'chinyengo.' Cholinga chimakhala chakuti chinthu cholakwika chiwoneke ngati cholondola. Mdyerekezi amafuna kuti anthu adzinama chifukwa iye amadana ndi chowonadi. Yesu anamutchula dyabulosiyu kuti ndi 'tate wa mabodza' (Yohane 8:44) Baibulo limati 'Musamupatse mpata Satana' (Aefeso 4: 27).

Anthu achinyengo amatha kupanga ndalama za mapepala ndi za chitsulo mwa chinyengo. Ndalamazi zimatha kuwoneka ngati zenizeni koma ziri zopanda mtengo. Oterewa nthawi zambiri amapezeka m'malire a dziko ndi kumagulitsa ndalama zawozi pa mitengo yotsikirapo.

Mwina akhoza kukhala wogulitsa magalimoto oti anagwiritsidwapo ntchito ndi anthu ena koma kuwagulitsa pa mtengo wokwera kwambiri. Nthawi zina anthu otere amanenakuti galimoto yawo ndi yabwino kwambiri iri yovutavuta. Kugulitsa chinthu choputaputa pa mtengo wokwera ndi chinyengo. Kunama si chinthu chabwino ayi. Ngati ife tidayamba tanamapo, tiyenera kulapa ndi kumupempha Mulungu kuti atikhululukire. Akulu a mipingo ndi anthu wochita bizinesi asamagwiritse ma udindo wawo kupezera ndalama kuchokera kwa anzawo. Iwo ayenera kupemphera kwa Mulungu kuti awapatse nzeru kuti adzilandira ndi kugwiritsa ntchito ndalama mowona mtima.

Nthawi zina anthu a bizinesi amayesayesa kuti apeze ndalama zambiri mu nira yosalungama – mwina polandira ziphuphu kapena kuyikapo tindalama towonjezera kuposera pa mtengo wa chinthu. Mwinanso mgwirizano wa ntchito (makontarakiti) umatha kusayinidwa koma uli wopanda chilungamo ndi wopondereza anthu antchito mpaka mwina kuwalowetsa mu ngongole yosayifuna. Mulungu sangadalitse mipingo, mabizinesi kapena mayiko odzaza ndi chnyengo kudzanso katangale.

Petro anamuwuza Hananiya kuti anali Satana amene adamupangitsa iyeyu kuti aname. Pamene Mulungu anali kulenga dziko lapansi anali kuganizira dziko lopanda uchimo, lopanda mavuto, lopanda njala, lopanda matenda, losamva zowawa ndi lopanda imfa. Iye anawona mayiko odzazidwa ndi ulemerero ndi mphamvu Yake! Atabwera Satana adadzayika chikayiko mu maganizo a Adamu ndi Hava pa chikhalidwe cha Mulungu. Ichi chinali chinyengo. Koma Mulungu anali atakonzeratu nzeru ina yomugonjetsera Satana. Iye adakonza kuti adzatumiza Mwana Wake ku dziko lapansi kuti kupyolera mu imfa ya Yesu ndi kuwuka Kwake mphamvu ya Satana idzathyoledwe. Izi zidzachitira ubwino iwo amene akhulupirira mwa Yesu atayitanidwa ndi Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera.

otsekedwa ndipo alonda anali chilondere koma mkatiomo munalibe aliyense' (5:23). Nthawi yonseyi Atumwi anali kufunidwawo anali kunja kulalikira mu dzina la Yesu monga momwe mngelo uja anawawuzira (5:23,28).

Atumwiwo anali kulalikira molimba mtima kwa anthu osonkhana pa bwalopo. Iwo anali ndi chikhulupiriro chokhazikika mwa Yesu. Anali kudziwa bwino lomwe tsopano chowonadi cha Yesu ndi chikonzero cha Mulungu kwa Ayuda (5:30-32)

Bwalo lija lidafuna kuwapha Atumwiwo, koma m'modzi wa atsogoleri dzina lake Gamaliyeri anati, 'Asiyeni amuna amenewa! Aloleni azipita…ngati kulalikira kwawo kuli kochokera kwa Mulungu, inu simungathe kuwaletsa iwo; motero inu mudzakhala mukukangana ndi Mulungu' (5:39) Mawu anzerutu awa!

Komabe bwalo lija lidalamula kuti Atumwiwo akwapulidwe. Adalamulanso kuti asamvenso Atumwiwo akutchula dzina la Yesu (5:40) Kenaka adawasiya kuti amuke, koma Atumwiwo adapitirirabe kuphunzitsa mu Kachisi (5:42). Iwo anali wodzaza ndi chimwemwendipo analinso kupita khomo ndi khomo (nyumba ndi nyumba) 'kulalikira Uthenga Wabwino wonena kuti Yesu ndiye Khristu'.

Mu mayiko ambiri a pa dziko lapansi mpingo wa Chikhristu wakhala ukukula mu nthawi ya manzunzo. Ngakhalenso lero, okhulupirira ambiri ali kundende. Ambiri ali kunzunzidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Ena amafa ndipo mizimu yawo imapita Kumwamba. Komabe Mulungu amatha kupulumutsa ndi kutsitsimutsa mwa zozwizwa za machiritso ndi mawomboledwe.

KAMBIRANANI

1. Ndi chifukwa chiyani Mulungu adaweruza Hananiya ndi Safira?
2. Kodi Mulungu amanena chiyani zakunena bodza (Aefeso 4: 25)?
3. Kodi nthano imeneyi imatilangiza ife chiyani monga Akhrisitu ponena kuti chikhulupiriro chathu chiyenera kutisiyanitsa ife ndi anthu ena?
4. Ndi chifukwa chiyani Atumwi anali wolimba mtima (5:29–32)?
5. Atumwi adachita zotani pamene anali kunzunzidwa (5:41, 42)?

WERENGANI : MACHITIDWE 6:1–15

KUKONZETSERA KUKULA KWA MPINGO

Anthu ambiri anali kulowa mu mpingo (6:1); chotero kunafunika kuti asankhe atsogoleri owonjezera. Panafunikanso anthu ena oti adzitsogolera ndi kuthandiza pankhani yogawana chakudya malinga ndi kukula kwa mpingo. Atumwiwo anafunsa okhulupirirawo kuti asankhe anthu asanu ndi awiri. Tawonani tsono m'mene anawasankhira:

- Iwo anawona kuti ntchito yotumikira anthu ena inali yofunika kwambiri.
- Iwo anasankha anthu amene anali ndi nzeru ndi wodzala ndi Mzimu Woyera (6:3).
- Iwo anawasankha oterewa kuti akagwire ntchito yothandizirayi ndi cholinga cha kuti Atumwi adzitha kulalikira utenga mosapingidwa ndi nkhani ya zakudya.

- Atumwiwo anasanjika manja awo pa anthu asanu ndi awiriwo napemphera nawo pamodzi (6:6).

Iyi inali njira yachirendo yosankhira atsogoleri popeza inasiyana ndi njira imene anasankhira Matiyasi pa Machitidwe 1:26.

Kodi chinachitika ndi chiyani anthu aja atatsata njita imeneyi pothandizira kukula kwa mpingo?

KUSANKHA ATSOGOLERI OYENERA

Kodi mpingo wanu umasankha bwanji atsogoleri ndi wogwira ntchito? Ndi anthu wotani amene mumawasankha?

- Kodi ndi anthu wokhala ndi chidziwitso, wokhulupirika, ndi wowopa Mulungu?
- Kodi ndi anthu amene amamudziwa Ambuye Yesu monga mpulumutsi wawo?
- Kodi ndi anthu amene khalidwe lawo ndi losachititsa manyazi? Kodi ndi anthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi akukhala nacho chidziwitso (Machitidwe 6:3)

Onanitu kuti Atumwi adawafunsa okhulupirira onse kuti awawthandize kusankha anthu ogwira ntchito. Izi zinali zokondweretsa ali yense (6:5).

1. Mpingo unakhala mpingo wokondwa (6:5).
2. Uthenga wa Mulungu, umene uli Uthenga Wabwino wa Yesu unapitirira kufalikira (6:7).
3. Chiwerengero cha okhulupirira mu Yerusalemu chinapitirira kukula.

KAMBIRANANI

1. Kodi okhulupirirawa anachita chiyani pokonzekera kukula kwa mpingo (6:1, 5, 6)?
2. Kodi atsogoleri a Mpingo anatenga mbali yotani pokonzetsera kukula kwa mpingo (6:2–4, 6)?
3. Kodi zotsatira za mpingo wokonda ndi wolinganizidwa bwino ndi zotani (6:7)?

NTCHITO NDI UMBONI WA STEFANO

Mulungu amagwiritsabe anthu wamba kuchita zinthu zodabwitsa. Ife tikamalalikira Uthenga Wabwino mwa Mzimu Woyera, Mulungu amayitana ndi kupulumutsa anthu ochimwa. Iye amawamasula ochimwawa ku nsinga za uchimo zimene zimawamanga. Mulungu amachita 'zizindikiro ndi zozizwa', ndipo Iye amachita izi kupyolera mwa wina aliyense amene Iye wamusankha. Iye amagwiritsa ntchito aliyense amene wafuna kuti amugwiritse ntchito (Ahebri 2:4).

Stefano anali munthu wamba koma 'anali wokhulupirira ndi wodzaza ndi Mzimu Woyera' (6:5, 8). Iye anali kuthandizira kugawa ndalama kwa osauka kuti akagulire chakudya. Mulungu anamugwiritsanso Stefano ntchito pochita zozizwa. Kuli konse kumene Stefano anali kupita anali kuwawuza anthu za Yesu Khristu ndi mphamvu Yake yakutha kupulumutsa anthu ku machimo

awo. Ena mwa atsogoleri a Chiyuda anakhulupirira nayamba kutsatira chiphunzitso cha Yesu (6:7).

Koma Ayuda ena ochokera ku Afirika ndi ku Asiya sanakondwere nazo. Zonena za Stefano zinali kuwakwiyitsa koma iwo sakanatha kutsutsa poti nzeru ndi chidziwitso chake zinali zopambana. Mwa njira ina Mzimu wa Mulungu anali kulankhula kupyolera mwa iye (6:10). Choncho iwo anagula anthu ena kuti afalitse mabodza ndi kukamunenera umboni wonama ku bwalo la mirandu (6:11, 13). 'Tanamumva iye akunenera Mose ndi Mulungu mawu amwano' iwo ananama. Stefano anali kunena za Mulungu koma iwo ananena kuti anali kunenera Mulungu za mwano. 'Kunenera Mulungu mwano' kunali kutanthawuza kuyankhula monyoza Mulungu (6:11). Izi zinawutsa mkwiyo wa atsogoleri a Chiyuda

CHIMWEMWE CHIFUKWA CHOFALITSA UTHENGA WABWINO

Atumwi anapeza chimwemwe choposa chifukwa chowawuza ena za Yesu. Uthenga Wabwino ndi nkhani ya Uthenga Wabwino wonena Za Yesu Khristu ndi chipulumutso Chake. Pauloananena kuti 'Uthenga Wabwino umawonetsera m'mene Mulungu amawalungamitsira anthu ndi kuwayanjanitsa ndi Iye (Aroma 1:17).

Ife timapulumutsidwa mwa nsembe ya Yesu. Iye analangidwa m'malo mwathu. Iyeyu amatipulumutsa ife ku imfa ndi kutipatsa moyo watsopano. Ife sitinayenera kulandira chikondi chotere. Palibe angapereke dipo la chikhululukiro ndi chipulumutso cha Mulungu. Ife tapulumutsidwa mwa chisomo basi- kukonda, chifundo ndi chisoni Chake. 'Mulungu anaconda dziko lapansi kotero, kuti anapereka (nsembe) Mwana Wake m'modzi yekha' (Yohane 3:16). Ife timapulumutsidwa pamene tikhulupirira kuti Yesu ndiye Khristu, Mwana wa Mulungu, amene adaphedwa m'malo mwathu (Aefeso 2:4,5,8,9).

- Uthenga Wabwino ndi yankho la Mulungu kapena makhwala ochizira tchimo.
- Uthenga Wabwino ndi kuyankhula kwa Mulungu konena kuti amatikonda ife.
- Uthenga Wabwino ndi nthano ya kudzipereka nsembe kwa Mulungu.
- Uthenga Wabwino unena za Yesu kunzunzidwa m'malo mwa ife.
- Uthenga Wabwino utanthauza kupulumutsidwa ku chilango.
- Uthenga Wabwino unena za chikhululukiro cha Mulungu kwa ife.
- Uthenga Wabwino ndi njira imene Mulungu ali kutibwezeranso ife kwa Iye mwini.
- Uthenga Wabwino umabweretsa mtendere ndi kutiyanjanitsa ndi Mulungu.
- Uthenga Wabwino umatimasula ife ku uchimo tinali kuchita kale.
- Uthenga Wabwino umapatsa mphamvu yakukhala m'moyo wachiyero,
- Uthenga Wabwino umapereka chiyembekezo chodzakhala mu moyo wosatha.

Uthenga Wabwino ndiyo mbiri yokoma ya zimene Mulungu anatichitira ife. Miyoyo yathu inasintha kotheratu. Ichi ndi chifukwa chimene chimatikakamiza kukhala okondwa pamene tiwawuza ena Uthenga Wabwino wa Yesu. Mulungu amadalitsa kulalikira kwa chowonadiChake poyitanira anthu kwa Iye mwini ndi kwa Mwana Wake. Imeneyi, ndiyo ntchito ya Mzimu Woyera.

WERENGANI: MACHITIDWE 7:1–60

STEFANO AYANKHULA KWA ATSOGOLERI A AYUDA

Mkulu wa ansembe ndiye anali kuweruza mu Bwalo la mirandu la a Yuda. Iye anamufunsa Stefano, 'Kodi zinthu izi ndi zowona?' (7:1). Stefano anamuyankha iye motere:

Choyamba anafotokoza mbiri ya Ayuda, m'mene Mulungu anaperekera malonjezo kwa Abrahamu ndi Mose. Mulungu adapereka malamulo kuthandiza mtundu wa Aisrael kuti umudziwe ndi kukhala moyo womusangalatsa Iye. Kenaka, Stefano ananena kuti Ayuda sanamvere Mzimu wa Mulungu. Mulungu anali kutumiza aneneri Ake koma Ayudawo anali kuwapha (7:51:52). Iwo sanamvere Malamulo a Mulungu, koma anali kupembedza Moleki, ndi fano la Amoni, ndi kupembedzanso nyenyezi za mulengalenga. Chifukwa cha ichi Mulungu analola kuti Ayuda atengedwe ngati akapolo kupita ku Babulo (7:43: Aroma 1:22-25). Stefano adawakumbutsa atsogoleri a Ayudawa zimene Mulungu anachita. Iye anati:

1. Anali Mulungu amene anamuyitana Abrahamu ndi banja lake kukakhala m'dziko limene Ayuda anali kukhalalo. (7:2-4).
2. Anali Mulungu amene anamulonjeza Abrahamu kuti banja lake lidzakhala mu dzikolo (7:5).
3. Ndi Mulungu yemweyo amene ananenanso kuti banja lake lidzakhala m'dziko la chirendo (ku Aigupto) zaka mazana anayi ndipo kenaka adzayesedwa akapolo, koma potsiriza pake adzabwereranso ku dziko lawo (7:6–7).
4. Anali Mulungu amene anayankhula kwa Mose mchitsamba choyaka moto. Mulungu anagwiritsa ntchito Mose kutululutsa anthu Ake mu Aigupto ndi kuwatsogolera ku dziko la lonjezano (7:30–35).
5. Anali Mulungu amene anamuwuza Mose za Mneneri (Mesiya) amene adzabwere (7:37).

Stefano anawawuza iwo kuti makolo awo sanamvere Mulungu (7:51) kapenanso kumumvera Mose ndi aneneri ena a Mulungu a nthawi yakale (7:52).

STEFANO APHEDWA

Stefano anawawuza Ayuda kuti anali ngati makolo awo, amene kalekale, anapha aneneri. Aneneriwa anali kulosera za kubwera kwa Mesiya – Mthenga wa Mulungu wopatulika. Stefano anawawuzanso kuti iwo anamupha Mesiyayo (7:52). Iye anali kutanthawuza Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu amene ndiye Mesiya.

Mawu amenewa adawakwiyitsa kwambiri atsogoleri a Ayuda. Iwo anakuwa namukwakwazira kunja kwa mzinda kuti akamugende miyala. Pamene anali kumugenda miyalayo Stefano anali kuwapempherera (7:60)

Mtsogoleri wina wa Ayudawo wotchedwa Saulo anali kuwonerera. Iye anavomereza kuti Stefano anayenera kuphedwa (8:1). Saulo anali mtsogoleri wa Ayuda wochenjera kwambiri, amenenso anali kudziwa malemba wopatulika.

Iyeyu koma, sanadziwe kuti Yesu anali Mesiya wolonjezedwayo.

Filipo anati, 'Tamupeza amene Mose analemba za Iye mu Chilamulo. Anenerinso analemba za Iye. Uyu ndi Yesu wa ku Nazareti' (Yohane 1:45). Ambiri mwa Ayuda anakhulupirira mwa Yesu.

KAMBIRANANI

1. Kodi m'neneri wolonjezedwa kuti adzabwera anali ndani (7:37)?
2. Kodi ndi ndani anapha aneneri zaka zambiri zapitazo (7:52)?
3. Kodi ndi ndani amene anapha mneneri amene Mose ananena za Iye (7:52)?
4. Ndi ndani amene sanamvera Malmulo a Mulungu (7:53; 8:1)?

WERENGANI: MACHITIDWE 8:1 – 25

MPINGO USAWUTSIDWA NDIPO UFALIKIRA KU MADERA ENA

Pa nthawi ija imene Yesu anali ndi Akuphunzira Ake anawawuza iwo kuti: 'Mudzaperekedwa kuti akakunzunzen inu ndi kukuphani . . .' (Mateyu 24:9). Ichi chimadziwika monga 'chisawutso'. Ataphedwa Stefano chisawutsochi chinayambika mu Yerusalemu. Pa nthawi imeneyi, Saulo anayesetsa kuletsa anthu kukhulupirira mwa Yesu. Iye adawaponyaambiri mu ndende, ndi kuphanso ena. Okhulupirira ambiri anasiya nyumba zawo mu Yerusalemu ndipo anapita kukakhala ku madera ena. Iwo anali kukamba za Yesu kulikonse kumene iwo anali kupita (8:4). Chisawutsochi chidathandizira kufalitsa Uthenga Wabwino ku madera ena a kutali.

Okhulupirira akunzunzidwa (kusawutsidwa) mu mayiko ambiri lero lino. Yesu anati, 'Ngati iwo adasawutsa Ine, adzasawutsanso inu' (Yohane 15:18). Ife sitiyenera kudabwa pamene tisawutsidwa. Tiyenera kuyma nji! Tiyenera kupempherera iwo amene akunzunzidwa kuti asataye mtima ndi kuleka kutsata njirayi.

ZOCHITIKA KU SAMARIYA

Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu udayamba kufalikira kuchokera ku Yerusalemu kufika ku mayiko ena. Yesu anati, 'Inu mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, mu Yudeya, mu Samariya ndi . . . Kuchokera mapeto ena a dziko kufikira mapeto enanso' (Machitidwe 1:8). Pa Machitidwe chaputala cha 8, tikuwerenga za m'mene Uthenga Wabwino unafikira ku Yudeya (8:1), Samariya (8: 1, 5, 25), Aitiopiya (8:27) ndi ku madera ena a Yudeya (8:40).

Filipo anali mtsogoleri mu mpingo wa ku Yerusalemu. Ayuda sanali kukondana ndi a Samariya, koma Filipo anapita ku Samariya kukalalikira za Yesu Khristu, amene alinso Mesiya, mu mzindawo. Mulungu anali naye ndipo iye anachita zozizwa zambiri mu dzina la Yesu (8:7-8).

Mwamuna wina wotchedwa Simoni amene anali wamatsenga anali kukhala mu mzindawo. Iye anali kuchita ndi kumawonetsa anthu za matsenga zake zoyipa. Anthu anali kumutchula kuti 'mphamvu yayikulu'. Koma tsopano anthu anayamba kukhulupirira mwa Yesu Khristu (8:12). Naye Simoni ananena kuti akukhulupirira mwa Yesu, choncho Filipo anamubatiza iye pamodzi ndi ena amene anatembenuka ndi kusiya machimo awo. Awa analapa ndipo anapulumutsidwa.

Atumwi a ku Yerusalemu anatumiza Petro ndi Yohane kuti akawone zimene zinachitika ku Samariya. Atumwiwa anapempherera Akhristu atsopanowa ndi kusanjika manja pa iwo 'ndipo analandira Mzimu Woyera' (8:15–17). Zambiri zozizwa zinachitika ndipo Simoni anawona zimene zinachitikzi. Iye analakalaka atakhala nayo mphamvu yonga imeneyi. Choncho iye anafuna kuti 'amugulitse mphamvuyi' kuti naye adzitha kuchita zodabwitsa (8:18). Koma iye anali ndi cholinga chiyipa.

'Kodi iwe uyesa ungathe kugula mphatso ya Mulungu ndi ndalama?' Petro

anamufunsa. Simoni anali asanatembenuke kwenikweni ndipo analibe chikhulupiriro chowona. Petro anamuwuza iye kuti atayike (kuwonongeka) ndi ndalama zakezo. Mulungu safuna kuti wina aliyense alangidwe. Iye afuna anthu onse akalape ndi kutembenukira kwa Yesu (8:21-23; 2 Petro 3:9). Simoni adamufunsa Petro kuti amupempherere pakuti njira zake zakale zinali kumulamulirabe.

Ngati inuyo njira zanu zakale ziri kukulamuliranibe, ndi chinthu chabwino kuwafunsa atsogoleri ampingo kuti akupemphereereni. Petro ndi Yohane anapitirza kulalikira pamene anali kubwerera ku Yerusalemu (8:25).

WERENGANI: MACHITIDWE 8:26 – 40

UTHENGA WABWINO KU AITIOPIYA

M'ngelo anadza kwa Filipo nati kwa iye, 'Nyamuka nupite mbali ya kumwera . . . mnjira yotsikira ku Gaza' (8:26). Filipo anasiya misonkhano yokoma ya mu Samariya nayenda molunjika ku Gaza kutsata msewu wopita ku ku Aigupto ndi Aitiopiya.

Tawonani galeta lokokedwa ndi akavalo (mahatchi) linali kudza potero. Filipo anawona mdindo wa ku Aitiopiya amene anali wotumikira mu nyumba ya Mfumukazi atakwera pa galetayo. Iye anali kuwerenga zolembedwa zopatulika.

© GRN

Mzimu wa Mulungu anati kwa Filipo, 'Yandikira nudziphatike ku galeta uyu'. Filipo atayandikira anamva kuti munthuyo anali kuwerenga mneneri Yesaya (Yesaya 53:7–8).



© GRN

UTHENGA WABWINO UFIKA KU AFIRIKA

Tawona m'mene mdindo wa m'nyumba ya ufumu ya Kandake adapulumutsidwira ndi Mulungu:

1. Iye anali wokhulupirira kale mwa Mulungu ndipo anafuna kukamupembedza Iye ku Yerusalemu (8:27).
2. Iye anali kuwerenga zolembedwa zopatulika (Chipangano Chakale) ndipo anali kufunitsitsa atazimvetsa (8:28, 31).
3. Mzimu Woyera anatuma munthu wina cut akamumasulire ulosi a Yesaya wokhudza Yesu (8:32, 34).
4. Munthuyu anakhulupirira Uthenga Wabwino wa Yesu ndipo anabatizidwa (8:35-38).

FUNSO : Kodi alipo anthu amene inu mukawadziwa amene ali kale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu koma asoweka kumvetsetsa Baibulo? Pempherani kuti Mzimu Woyera atumize munthu odzawathandiza kumvetsetsa ndi kukhulupirira kuti Yesu ndiye Mpulumutsi. Izi zidzawapatsa iwo chimwemwe choposa.

Flipo anamufunsa mdindoyo kuti, 'Kodi muzindikira chimene mukuwerenga?' 'Ndingathe kuzindikira bwanji popanda ondimasulira?' anayankha m'dindoyo.

Popanda Mzimu wa Mulungu kutithandiza, ife sitingathe kulimvetsetsa Baibulo (1 Akorinto 2:14). Chotero Mulungu amatipatsa ife Mzimu Wake kuti atiphunzitse chowonadi (Yohane 16:13–14). Pamene tikufuna kuwerenga Baibulo, tiyenera timufunse Mulungu kuti atithandize kumvetsetsa mawu Ake. Timupemphe Iye kuti atipatse chimwemwe pamene tiwerenga bukhu Lakeli (8:39). Timupemphe kuti athe kutumiza anthu ena kudzatithandiza kumvetsetsa ndi kuti tidzagawane nawo chimwemwe chochokera ku mawu Ake.

Mulungu adamutuma Filipo kuti amuthandize munthu uja. Filipo adamuwuza mdindo uja kuti Yesaya analemba za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu ngakhale anali pa dziko zaka mazana asanu ndi awiri Yesu asaanabadwe ku Betlehemu. Mdindo uja atamva izi anakhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Anamupempha Filipo kuti amubatize, ndipo atamubatiza Mzimu Woyera anakwatula Filipo. Mdindo uja anapitirira ulendo wake wobwerera kwawo ku Aitiopiya. Anali nawo udindo wokafotokozera ena za zimene anazimva kunyumba kwa Mfumukazi (8:27, 39).

Anthu ena amakhulupirira kuti iyeyu anali wotembenuka (Mkhristu) woyamba kum'mawa kwa Afirika. Anabwerera kwawo ali 'wokondwa' (8:39) kukwuza ena za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Munthu wa ku Aitiopiya yu anakhulupirira chifukwa chowerenga mawu a Mulungu komanso atalandira thandizo kuti athe kumvetsetsa.

KAMBIRANANI :

1. Kodi chidachitika ndi chiyani okhulupirira atayamba kunzunzidwa (8:1-8)?
2. Kodi chinali kumulepheretsa Simoni wamatsenga uja kuti akhulupirire ndi chiyani (8:19–23)?
3. Inuyo kodi mumawawuza ena za Uthenga Wabwino mukakhala pa ulendo (8:25)?
4. Kodi anthu achite chiyani kuti apulumutsidwe (8:26–40)? Nanga Mulungu amachita Chiyani kuti awapulumutse?
5. Kodi mumatha kugawana ndi ena chowonadi cha Mulungu chochokera mu mawu Ake a mu Baibulo?

WERENGANI: MACHITIDWE 9:1 – 43

SAULO AKUMANA NDI YESU

Panthawi yamasawutsoyi, Akhristu okhulupirira anali atayenda mpaka kukafika ku Damasiko mdziko la Suliya. Saulo, m'modzi wa atsogoleri a Chiyuda anapempha makalata omulola kuti akaponye okhulupirira onse mndende (9:2). Anthuwa anali kumuwopa Saulo.

Saulo ananyamuka ulendo wopita ku Damasiko kukasaka Akhristu kuti akawamange mu matangadza. Palibe akadakhoza kumuletsa koma Mulungu yekha. Pamene anali kuyenda atakwera pa kavalo wake, kuwala kwakukulu



kunamukuta ndi kukantha maso ake. Ndipo anamva mawu ochokera kumwamba akunena, 'Saulo, Saulo, undilondalonderanji?' Iye anagwa pansi panjira pomwepo.

'Ndinu yani Mbuye?' iye anafunsa. Ndipo mawuwo anapitirira nati, 'Ndine Yesu amene umulondalonda'. Anzake amene anali naye anafika panali iye namunyamutsa, ndipo tawonani kuti anali atachita khungu. Choncho anamulondolera njira kufika ku Damasiko kumene anakhala masiku atatu ali wosapenyabe. Ndipo sanadya kapena kumwa koma anangodikira Mulungu kuti amuwuze choyenera kuchita.

Kumbali ina ya mzindawo kunali wokhulupirira wina wotchedwa Hananiya. Mulungu anyankhula naye ameneyu nat, 'Uka upite kunyumba ya Yuda… ndipo ukafunse za munthu dzina lake Saulo wa ku Tariso . . .' (9:15).

Hananiya anali kudziwa kuti Saulo anali kupha Akhristu ku Yerusalemu ndipo anachita mantha. Koma Mulungu anati, 'Usawope. Ndamusankha munthu ameneyo kuti andigwirire ntchito Ine. Iye atuluka kupita kwa amitundu ndi kwa mafumu awo kukawawuza za Ine' (9:15).

Hananiya anakampezadi Saulo monga m'mene Mulungu ananenera, ndipo anamupempherera iye. 'Mbale Saulo, Ambuye wandituma ine, ndiye Yesu amene anakuwonekerani panjira wadzerayo, kuti upenyenso ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera.'

Nthawi yomweyo Saulo anapenya! Iye anakhulupirira Ambuye Yesu Khristu ndi kubatizidwa. Zitachitika izi anadya chakudya.



SAULO AYAMBA MOYO WATSOPANO

Saulo anali kumudzuiwa Mulungu koma sanakhulupirire kuti zolembedwa zopatulika zinali kunena za Yesu, amene ndi Mesiya. Chidamuwonekerachi chinali chozizwa chochokera kwa Mulungu. Kuyambira pa nthawi imeneyi Saulo anakhulupirira Yesu anali 'Mwana wa Mulungu.' Saulo anapulumutsidwa mwa chisomo cha Mulungu ndi mwa chikhulupiriro chake mwa Yesu. Chikhulupiriro chake mu Malamulo a Mose sichinali chokwanira kumupulumutsa iye.

Saulo analowa mu Sunagoge nalankhula kwa anthu m'menemo. Anali atasanduka munthu wosinthika. Iye anawawuza anthu za 'Yesu Mwana wa Mulungu' (9:20). Ulaliki ndi chiphunzitso chake zinali kukulirakulirabe (9:22) ndipo anthu anati, 'Tsopano akulalikira za chikhulupiriro chimene anafuna kuchiwononga' (Agalatiya 1:23).

Ayuda a ku Damasiko anali kulephera kutsutsana naye Saulo chifukwa cha mawu ake amphamvu choncho anakonza chiwembu kuti amuphe. Iwo anayang'anira pa zipata usiku ndi usana kuti amugwire akamadutsa. Akhristu ena atamva izi anamutsitsira iye kunja kwa mzinda kudzera pa zenera la linga atamukhazika mu mtanga (9:25). Saulo mwini anafotokoza nkhani imeneyi pa Agalatiya 1:11-24; 2:1.

Kenaka Saulo anapita ku Yerusalemu kumene anayesayesa kulumikizana ndi akuphunzira ena, koma iwowa anali kumuwopa iye. M'modzi wa akulu ampingo otchedwa Barnaba, anamutengera iye kwa Atumwi, nawafotokozera zimene zinamuwonekera Saulo pa njira ya ku Damasiko.

Kuchokera tsiku limenelo, Saulo 'analankhula molimba mtima mdzina la Ambuye.' Iye analankhula mopanda mantha ndipo ukunso Ayuda anafuna kumupha. Ena mwa okhulupirirawo anamutengera iye ku doko la Kaisareya ndipo anamutumiza iye pa bwato ku ku mudzi wa kwawo ku Tariso (9:30). Tariso unali mzinda wopezeka ku Asiya (Kilikiya). Panthawiyi Mulungu anakhazikitsa mpingo ku dziko la pakati cha kum'mawa umene unali wolimba ndi wamphamvu. Okhulupirira anakhala nayo nthawi ya bata ndipo anthu ambiri anakhala akhristu (9:31).

KAMBIRANANI :

1. Kodi Mulungu adamusintha bwanji Saulo (9:6–16)?
2. Ndi chiphunzitso chotani chimene mpingo uyenera kuwapatsa anthu okhulupirira kumene (9:15–20).
3. Kodi ndi chifukwa chiyani Ayuda anali kufuna kumupha Saulo (9:23, 29)?
4. Kodi Barnaba anamuthandiza bwanji Saulo?
5. Chinachitika ndi chiyani kwa okhulupirira a Chikhristu (9:31)?
6. Kodi Saulo chinamuchitikira ndi chiyani (9:30)?
7. Ndi chifukwa chiyani kuli kofunika kuti tidzimvetsetsa Baibulo?

AYUDA AWONA MPHAMVU YA YESU

Petro sanali kukhalitsa mu Yerusalemu. Tsiku lina anapita ku Luda kumpoto

cha kumvuma kwa kwa dziko la Israeli. Mu mzinda umenewu, Petro anakumana ndi munthu dzina lake Eneya amene anali atadwala nthawi yayitali. Petro anamuchiritsa iye mu dzina la Yesu. Motero Ayuda onse a mumzindawu anakhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu (9:35).

Anthu ambiri amene amakhala madera oyandikira anakhulupiriranso. Dorika anali kukhala ku Yopa. Iye anadwala ndi kumwalira. Okhulupirira anatumiza mthenga kwa Petro msanga. Petro anakumbukira m'mene Yesu anawukitsira anthu atatu kwa akufa (Mateyu 9:25; Luka 7:11–17; Yohane 11:1–44). Petro anafika kunyumba kwa Dorika ndipo anawatulutsa anthu onse m'nyumba m'mene anagonekedwa wakufayo. Iye anagwada pansi ndi kupemphera. Mayiyo anawuka nakhala moyo. Zitachitika izi anthu ambiri mu Yopa anakhulupirira mwa Ambuye Yesu.

Petro anakhala mu Yopa kwa masiku angapo ali kulalikira ndi kuphunzitsa anthu. Ndi nthawi imeneyi imene Mulungu adamuwonetsa kuti anayeneranso kulalikira kwa amitundu.

WERENGANI: MACHITIDWE 10:1 – 48

PETRO ACHEZERA MUNTHU AMENE SANALI MUYUDA

Aroma anali kulamulira Israeli, choncho asilikari a Chiroma ochokera ku Taliyana anali kukhala m'malo awo ankhondo mdzikoli. Gulu la asilikali a Chiroma amakhala m'magulu m'magulu a asilikali zana limodzi. Mkulu wa gulu lirilonse anali kutchedwa 'Kenturiyo' (Centurion) (Luka 7:2). Magulu oterewa okwana khumi amapanga gulu limodzi la anthu chikwi (Regiment) limene limakhala ndi dzina. Korneliyo anali kuytang'anira limodzi la magulu oterewa lotchedwa la Italiya. Iye ndi banja lake sanali Ayuda ayi, koma anali kukhulupirira ndi kupembedza Mulungu. Iwo sanali kumudziwa Yesu.

Tsiku lina, pamene Korneliyo anali kupemphera, anawona mngelo wa Mulungu. 'Mufuna chiyani Ambuye?' iyeyu anafunsa. Ndipo mngeloyu anamupatsa uthenga wakuti: 'Tumiza amuna ku Yopa akayitane munthu wotchedwa Petro. Iye akukhala kunyumba kwa Simoni wa zikopa' (10:6–7).Korneliyo anamvera natumiza anthu ku Yopa.

Naye Petro ali ku Yopa anawona anamuwonekera masomphenya ochokera kwa Mulungu. M'mene anali kupemphera, iye anamva njala. Kenaka anawona chotengera chokhala ngati nsalu yayikulu chikutsika pansi kuchokera Kumwamba. M'menemo munali nyama zambiri zodetsedwa – mbalame ndi zinyama zokwawa- zimene Ayuda sanali kuloledwa kudya kapenanso kuzikhudza. Ndipo anamva mawu onena kuti 'Ipha nudye.' Petro anayankha kuti, 'Sindinadyapo ine ndi kale lonse kanthu wamba ndi konyansa.' (10:14). Mawuwo anapitirira ndi kuti: 'Chimene Mulungu anayeretsa usachiyesa chinthu wamba.' (10:15). Mawu amenewa anali kuchokera Kumwamba ndipo anamufikira katatu.

Pamene Petro anali kusinkhasinkha za zinthu izi, amuna otumidwa ndi Korneliyo aja anafika ku nyumba kwa Simoni nafunsa kuti awonane ndi iye Petro. Mzimu Woyera anayankhula ndi Petro kuti, 'Usawope, nyamuka numuke nawo pakuti ndawatuma ine.' (10:20).

Tsiku lotsatira, Petro anapita ndi anthu aja ku Kaisareya. Lamulo la Chiyuda linali kuti mYuda asalowe m'nyumba ya munthu aene sali mYuda,



koma Mulungu anali ndi uthenga wakuti – Iye Mulungu, akhoza kuyeretsa china chiri chonse (10:15, 28). Palibe munthu wovuta woti Mulungu sangathe kumupulumutsa ayi! Iye anapulumutsa Saulo. Anali kufuna kupulumutsanso Korneliyo. Ayuda anali kunena kuti anthu amene sanali Ayuda anali 'odetsedwa', koma Mulungu anafuna kuti ngakhale amenewo ayenera kumva Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Petro anamuwuza Korneliyo kuti: 'Tsopano ndadziwa kuti Mulungu sakondera aliyense, koma akufuna anthu ochokera ku mtundu yonse' (10:34–35).

Kornrliyo ndi banja lake atamva za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, anakhulupirira. Mzimu Woyera anatsika nafika pa aliyense wa iwo ndipo analemekeza Mulungu mu zinenero (malirime) zochuluka (10:45–46). Kenaka Petro anawabatiza iwo 'mu dzina la Yesu Khristu.' Mzimu Woyera adadza pa iwo monganso adachitira pa tsiku la Pentekoste. (Machitidwe 2).

KAMBIRANANI :

1. Ndi chifukwa chiyani Mulungu adapulumutsa Korneliyo (10:2-4, 34)?
2. Kodi ntchito ya Mzimu Woyera mu chaputala 10:44-46 iri chimodzimodzi ndi muchaputala 2:4?
3. Kodi Mulungu akhoza kupulutsa aliyense amene Iye wamusankha?

WERENGANI: MACHITIDWE 11:1 – 30

PETRO ABWERERA KU YERUSALEMU

Akhristu Achiyuda a Muyerusalemu sanakondwe nazi zimene zimene Petro adachita. 'Iwe unalowa m'nyumba ya anthu amene si Ayuda ndi kukadya nawo pamodzi,' iwo anamudzudzula (11:3). Petro anaswa lamulo la Ayuda!

Koma Petro anawuza atsogoleri ampingo za masomphenya ake ndi zimene zinachitika mu Yopa. Iye anawawuza zimene Yohane M'batizi anali kunena Yesu asanayambe utumiki Wake: 'Iye (Yesu) adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera' (Marko 1:8).

Petro anawawuza atsogoleri ampingowo kuti Mzimu Woyera anadza pa anthu amene sali Ayuda 'monga m'mene adatsikira pa ife pa chiyambi paja' (11:15), iye asanawabatize anthuwo. Atamva izi onse analemekeza Mulungu pamodzi (11:18).

Ili linali lonjezano la Yesu Kwa onse amene akhulupirira Uthenga Wke Wabwino (Yohane 14:15–18).

M'MENE MPINGO WOYAMBA UDAFALITSIRA UTHENGA WABWINO

Pa nthawi imeneyi okhulupirira ena anali atayenda kudutsa Ufumu wa Aroma. Poyamba, iwo anali kulalikira Uthenga Wabwino wa Yesuwu kwa Ayuda (11:19). Kenaka ena a iwo anayamba kulalikira anthu amitundu (11:20). Okhulupirira a ku Kupro ndi ku Krene (Libya) anadza kudzakhala mu Antiokeya mu dziko la Asiriya. Antiokeya unali mzinda wa chitatu kukula mu Ufumu wa Aroma. Uku ndi kumene okhulupirira anatchedwa 'Akhristu' kwa nthawi yoyamba. Mulungu anali nawo ndipo anthu ambiri anakhulupirira nakhala akhristu. (11:21).

Pamene mpingo wa ku Yerusalemu unamva za izi unatumiza Barnaba ku Antiokeya kukawalimbikitsa aklhristu atsopanowo. Atachoka uku, Barnaba anapita ku Tarisi kumene anakamutenga Paulo kubwera naye ku Antiokeya kuti adzathandizane naye (11:25-26). Kuphunzitsa anthu amene angotembenuka kumene ndi ntchito yofunika kwambiri. Iwo asoweka kuthandizidwa kuti asinthe njira zawo zakale. Izi zingatheke pamene iwo amvetsera aphunzitsi odziwa bwino ndi kuphunzitsidwa zimene zimamukondweretsa Mulungu zochokera mu Baibulo ndi kutsatira ziphunzitso za Yesu.

Agabusi, mneneri wa ku Yerusalemu anabweranso ku Antiokeya. Mzimu Woyera anayankhula kupyolera mwa iyeyu za njala imene idzakhala mu ufumu wa Aroma wonse. Izi zinachitikadi mu nthawi ya Mfumu Karodiya (41-45AD). Pofuna kuthandiza anzawo a njala, okhulupirira adasonkha ndalama nawapatsa Barnaba ndi Paulo kuti akapereke monga mphatso ku mpingo wa ku Yerusalemu (11:29-30)

KAMBIRANANI

1. Kodi ndi chifukwa chiyani Akhiristu a Chiyuda adamupeza Paulo wolakwa?
2. Kodi inu ndinu wokonzeka kuyankhula za Mulungu kwa anthu akhungu losiyana ndi lanu kapena a chikhalidwe ndi zinenero zina?
3. Ngati Mulungu amatiwona tonse chimodzimodzi, kodi ife tiyenera kuchita mosiyana? (10:34) Kodi izi zitanthawuza kuti anthu onse ali chimodzimodzi?
4. Kodi Petro adakhoza bwanji kuyanjanitsa mpingo (11:17)?

WERENGANI: MACHITIDWE 12:1 – 25

MNGELO ATHANDIZA PETRO KUTHAWA MU NYUMBA YA NDENDE

Boma la Aroma lidakhazikitsa Herode Agiripa kukhala wolamulira dera la Yudeya. Iyu anali mdzukulu wa Herode wankhanza uja amene adalamula kuphedwa kwa ana wamuna a mu Betelehemu m'masiku a kubadwa kwa
Yesu (Mateyu 2:16).

Herode Agiripayu anaponya Akhristu ambiri mu ndende komanso anapha Yakobo m'bale wa Yohane (12:2).



Zimenezi zinawasangalatsa atsogoleri a Chiyuda, ndipo Herode angwiranso Petro namuponya mndende. Iye anali kufuna kuti adzazenge Petro mulandu ikadutsa nyengo ya masiku a mkate wopanda chotupitsa (12:4).

Koma Mulungu, Wolamulira wamkulu anafuna kuwonetsa kuti Iye ali ndi mphamvu zoposa za Herode. Herode sangathe kuchita kanthu pa anthu Ake ngati Iye sanalore. (1 Yohane 4:4).

Mu ndendemo, Petro anali womangidwa maunyolo molumikizana ndi asilikali awiri. Koma nthawi ya usiku pamene Petro anali kugona tulo kuwala kwadzidzi kunawalira chipinda cha ndende chonse, ndipo m'ngelo anamudzutsa iye ndi kunena kuti: 'Uka msanga. Tenga zovala zako ndipo unditsatire ine' (12:8).

Nthawi yomweyo unyolo unagwa pansi kuchoka m'mikono mwake ndipo iye anatsatira mngelo uja. Awiriwa anayenda pamodzi nadutsa alonda amene anali kulondera nyumba ya ndendeyo ndi kutuluka pa zipata za mzindawo.

Petro sanamvetse kuti chinali kumuchitikira ndi chiyani kufikira nthawi imene mngelo anamuchokera. Pozindikira kuti sanali maloto ayi, iye anafulumira napita kunyumba ya Mariya kumene anapeza Akhristu anzake akumupempherera iye (12:12). Poyamba iwo sanamuzindikire iye ndikukhulupirira kuti mapemphero awo



ayankhidwa (12:15).

'Kawuzeni Yakobo ndi Abale ena za zimene zandiwonekerazi,' Petro anawawuza Ahristuwo kenaka ndi kuchokapo.

ayankhidwa (12:15).

'Kawuzeni Yakobo ndi Abale ena za zimene zandiwonekerazi,' Petro anawawuza Ahristuwo kenaka ndi kuchokapo.

Herode anapha alonda a kundende aja chifukwa choti Petro anathawamo. Atatero Herodeyu anapita ku Kaisareya kukayendera anthu pa ntchito ya boma. Kumeneko anakhala pa mpando wake wolemekezeka nayamba kuwayankhula anthu amene adasonkhanapo. Ena mwa khamulo anayamba kukuwa ndi kumati: 'Awa ndi mawu a mulungu osati munthu.' Ichi chinamuyipira Mulungu ndipo mngelo wa Yehova anamukantha iye chifukwa sanapereke ulemerero kwa Yehova (12:22–23). Herode anafa mchaka cha AD 44, koma uthenga wa Mulungu unafalikira ku madera ena ndi ena.

KAMBIRANANI:

1. Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Paulo anali mu ndende (12:6–10)
2. Kodi mapemphere amawathandiza bwanji anthu amene azingidwa ndi makoma andende?
3. Nanga pemphero lingawathandize bwanji anthu amene akodwa mu umphawi, mu matenda ndi amene akuwopa?
4. Kodi mngelo wa Mulungu adamukantha motani Herode (12:33)?

KUWOMBA MKOTA (KUMALIZA)

Machitidwe a Atumwi nthawi zambiri amatchulidwanso 'Machitidwe a Mzimu woyera.' Luka analemba bukhuli kuti anthu adziwe ntchito zazikulu zimene Mzimu wa Mulungu anachita mwa Atumwi. Mumasiku oyambirira a mpingo wa Chikhristu, okhulupirira anali kugawana Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu mu mayiko onse a Pakati cha Kum'mwa (Middle East). Filipo anamuwuza munthu wa ku Afirika Uthenga Wabwino. Mabukhu a Mbiri Yakale amatiwuza kuti Marko anatengera Uthenga Wabwinowu ku Aigupto ndipo Tomasi anakawufikitsa ku India kumene unafalikiranso. Saulo anautengera Uthengawu ku Ulaya (Europe).

Mu masiku oyambirira a mpingowu Akhristu anali kunzunzidwa nthawi zina koma iwo analimbika, nawonetsa chikondi ndi kusamalira ena. Iwo sanali kuchita nkhondo akakhala m'mavuto. Ena anali kungosamuka, koma kumene anali kupitako anali kuchitira umboni za kuwuka kwa Ambuye Yesu mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Iwowa anali kukumana ndi Ayuda amene anali kukhulupirira Mulungu Wowona koma sanali kudziwa kuti Yesu Khristu ndiye Mwana wa Mulungu. Ambiri mwa iwowa anatembenuka nakhala Akhristu. Inalitu nthawi imeneyi pamene okhulupirira anayamba kudziwika ndi dzina lakuti 'Ahkristu'. Mzimu Woyera wa Mulungu anali kugwira ntchito mu miyoyo yawo. Iwo anapulumutsidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo mwa Yesu.

Tawerengatu za anthu atatu odziwika kwambiri amene anatembenuka pa nthawi imeneyi:

- Munthu wa ku Aitiopiya amene anakhulupirira Mulungu ndipo anafuna kumvetsetsa za Mesiya zonenedwa mu Zolembedwa Zopatulika za Ayuda (Chipangano Chakale).
- Saulo amene anakhulupirira Mulungu koma sanali kukhulupirira kuti Yesu anali Mesiya.
- Korneliyo amene anakhulupirira Mulungu ndi kumupembedza Iye koma anali asanamve za Yesu.

Mulungu anawakonda anthu amenewa kotero kuti Mzimu Woyera anatsogolera Filipo, Hananiya ndi Petro kukawathandiza. Iwo atamva ndi kuwumvetsetsa uthenga wa Yesu anakhulupirira mwa Iye ndipo anapulumutsidwa.

Mu njira yomweyi, Mulungu akufuna ifenso tiwawuze ena za Yesu Khristu. Kodi inu mumadziwa wina amene amakhulupirira Mulungu, koma sadziwa

kuti angapulumutsidwe bwanji? Funsani Mziu Woyera kuti akutsogolereni inuyo kuti mukathe kuwawuza iwo za Yesu Khristu.

Mu bukhu la 'Ndemanga Za Baibulo' lotsatira (la Machitidwe Gawo Lachiwiri) mudzaphunzira m'mene Mzimu Woyera anatsogolera Saulo amene anadzatchdwa Paulo kupita kwa anthu amitundu, ku mayiko ena. Anthu amenewa sanali kumudziwa Mulungu ayi ndipo ambiri anali kukhulupirira mafano ndi milungu yonama. Koma kupyolera mu kuphunzitsa ndi kulalikira kwa Paulo ndi mphamvu ya Mzimu Woyera ambiri anatembenuka ndi kukhala Akhristu. Iwo anapulumutsidwa ku machimo awo.

Tonsefe tiri ndi mbali imene tikhoza kutenga pa Chikonzero cha Mulungu chopulumutsa dziko. Mu m'badwo uli wonse ndi nyengo iri yonse anthu ambiri akubadwa amene sanamvepo za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Yesu anaphunzitsa kuti m'badwo uli wonse 'uyenera kubadwa mwatsopano' (Yohane 3:3). Choncho mu m'badwo uli wons Akhristu ayenera kusenza udindo wokafotokozera dziko lapansi za Yesu Khristu. Ife pamene tiyika chikhulupiriro chathu mwa Yesu Khristu ndi kubadwa mwatsopano Mulungu akufuna kuti tiwawuze ena za Uthenga Wabwino. Tikhoza kutsogozedwa pa ntchito imeneyi ndi Mzimu Woyera monga m'mene zidakhalira ndi Paulo mu masiku oyambirira a mpingo. Werengani Machitidwe Gawo Lachiwiri (machaputala 13 mpaka 28) m'mene mukunenedwa za m'mene Chikhristu ndi Uthengawu udafalikira ku dziko lonse la pansi. Izi zinachitika mu zaka makumi anayi, Kachisi Wamkulu wa ku Yerusalemu asanagwetsedwe mu AD70.

Iyi ndiyo ntchito ya Mzimu Woyera. Chimenechi ndi chifukwa chimene inu muyenera kuphunzira bukhu la Machitidwe a Atumwi. Potero mutha kumvetsetsa m'mene Mulungu akufunira kuti mudzikhalira lero motsogozedwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

Lero, anthu miyandamiyanda (2 billion) pa dziko lapansi amadzitchula 'Akhristu'. Mu chaka chiri chonse pali anthu amayereyere (oposa 50 million) amene ali okhulupirira. Chimene akusoweka ndi kuti 'abadwenso mwatsopano' pa kuphunzira, kukhulupirira ndi kukhala m'moyo wotsata chiphunzitso cha Yesu. Anthu asoweka kuphunzitsidwaza miyoyo ndi zolembedwa za okhulupirira a mu mpingo oyambirira. Ayenea kuwuzidwa kuti kulondola ndi kuti komanso kuphophonya ndi kuti.

Choncho tikukukakamizani kuti mudziwerenga Baibulo lanu tsiku ndi tsiku. Ndemanga za Baibulo zochokera ku Manna zikuthandizani kumvetsetsa Baibulo ndiponso kukthandizani inu kuphunzitsa ena za 'Chowonadi cha Mulungu.'

ANTHU OLUMALA KUPEMBEDZA MULUNGU

Atsogoleri a Chiyuda sanali kulola anthu olumala kulowa mu Kachisi ku Yerusalemu. Mkulu wa mpingo wolumala sanali kuloledwa kupereka nsembe (Levitiko 21:17–24). Koma Yesu anawawuza kuti Kachisiyu adzaphwasulidwa posakhalitsa (Marko 13:2). Nthawi idzafika posachedwa pamene anthu sadzapembedza Mulungu pa phiri lopatulika mu Yerusalemu (Yohane 4:21). Anthu adzamupembedza Mulungu mu 'mzimu ndi mu chowonadi' (Yohane 4:24) Ichi ndi chifukwa chake chimene tsopano lino anthu ali ndi ufulu womupembedza Mulungu ali pena pali ponse, pa nthawi ina iri yonse; anthu monga inu ndi ine; anthu ochimwa amene akudziwa kuti Mulungu adawakhululukira kupyolera mwa Yesu Khristu.

Ngakhale anthu olumala ali wolandiridwa. Wopemphetsa wolumala pa Machitidwe 3:8 anali wokondwa kwambiri atawona kuti akhozanso kuyenda ndi kulowa mu Kachisi kukamupembedza Mulungu. Iye anadziwa kuti palibe adzamutsekerenso kunja. Tchalitchi cha Yesu Khristu chimalandira munthu aliyense. Palibe amatsekeredwa kunja. "Ine ndidzawapanga olumala kukhala anthu anga okhulupirika' (Mika 4:7). Kodi mpingo wanu umawathandiza olumala kumupembedza Mulungu mosavutikira? Kumbukirani kuti Mulungu sawawona iwowa ngati olumala ayi. Ife titamawatengera olumala ku misonkhano yathu ena a iwo angathe kuchiritsidwako, pamene ena angathe kupulumutsidwako ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera amene akugwira ntchito pakati pa anthu a Mulungu. Mulungu akuchita zimebezi kupyolera mu dzina la Mwana Wake Yesu Khristu.

{Acts Part 1 1e 2004 Chichewa]

Wofalitsidwa ndi:

Lofalitsidwa ndi:

Manna Publications (UK)

Typeset ndi:

Manna Publications (UK)

God has enabled over 750,000 Manna Bible teaching commentaries to be printed and distributed in:

Angola, Armenia, Benin, Bulgaria, Burkina Faso, Burundi, Cambodia, Cameroon, Chad, Congo Dem. Rep. (Kinshasa and Katanga), Congo Rep. (Brazzaville), Egypt, Equatorial Guinea, Ethiopia, Ghana, Guatemala, Haiti, India, Ivory Coast, Kenya, Kosovo, Liberia, Malawi, Mali, Mexico, Mongolia, Mozambique, Myanmar, Nepal, Niger, Nigeria, Pakistan, Rwanda, Serbia, Sierra Leone, South Africa, Sudan, Swaziland, Tanzania, Togo, Uganda, Zambia and Zimbabwe

and in 43 languages including 2 in Braille

Download more Bible teaching commentaries from Manna Publications (UK) in English at: **www.manna-publications.org.uk**
Also in French, Portuguese and Spanish

Parent organisation Manna Publications (USA): **www.mannapublications.org**
Affiliated to **Avail**, UK registered charity 1017386

MACHITIDWE A ATUMWI: Mpingo woyambirira

BUKHULI Likutiphunzitsa za masiku oyambirira a Mpingo wa Chikhristu pafupifupi za zikwi ziwiri zapitazo. Uthenga Wabwino wakuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu unafalikira ku mayiko ambiri a pa dziko lapansili. Otsatira a Yesu analalikira Uthenga Wabwinowu mwa mphamvu. Mphamvu imeneyi inali ya Mzimu Woyera wa Mulungu imene inali kugwira ntchito kupyolera mwa omutsatira Yesuwa. Zinthu zambiri zodabwitsa zinawoneka.

MANNA PUBLICATIONS imafalitsa Ndemanga za Baibulo zolembedwa ndi a Fred Morris. Kwa zaka zambiri a Morris ndi mkazi wawo Lorna, azungulira dziko lapansi kuphunzitsa ndi kulalikira. Iwo atabwerera kumudzi kwawo anayamba kulemba ndemangazi kuti akazisindikize ndi kumazigulitsa kumene anthu akusowa maphunziro ngati amenewa.

BUKHU lobwerezedwali lidalembedwa mu chinenero chosavuta kuwerenga (Chingerezi chophweka choyankhulidwa pa dziko lonse) kuti lithe kuwonjezera kumvetsetsa ndi kufulumiza kutanthawuzira mu zinenero zina. Bukhuli limapereka maphunziro oyambirira kwa owerenga komanso maphunziro owonjezera kwa ophunzira Baiblo ngakhalenso aphunzitsi ndi Abusa.

MABUKHUWA mukhoza kuwagwiritsa ntchito pa nokha kapena pamene mukuphunzitsana pagulu. Ndi mabukhu ophunzitsa chowonadi cha Mulungu. Adzakuthandizaninso kumudziwa Yesu Khristu amen ali Mwana wa Mulungu ndi kukuthandizxani kukamba za chikhulupiriro chanu mwa Mulungu. Ndi othandizanso kuti musasokere pa moyo wanu wa uzimu pokudziwitsani zinthu zimene Mulungu amazikonda ndi zimene zimamunyansa.

PEMPHERO lathu ndi lakuti inu mukhale nawo mtendere watsopano ndi cholinga chokhazikika mu moyo wanu pamene mukuwerenga Baibulo ndi kugwirtsa ntchito ndemangazi.

Manna Publications

Chowonadi cha Mulungu ndi chinsinsi chodabwitsa ndi vumbulutso monga manna ochokera Kumwamba